Tiyeni tilipenyetsetse bwino pempheroli. Lili ndi zigawo zambiri. Ngati titadziŵa zigawo zimenezi ndiye kuti tidzakhoza kuligwiritsa ntchito pemphero limeneli mwakulimvetsetsa. Tingathe kupanga mapemphero athuathu pakugwiritsa zigawo zimenezi.

Atate Wathu Muli Kumwamba.

Chigawo chimenechi chimatiuza amene tili kulankhula naye pamene tili kupemphera. Chimatiuzanso mmene tingamuganizire. Iye ndi Atate wathu. Kumene kuli kutanthauza kuti amatisamalira ndi kutikonda. Koma ganizirani kuti tingathe kumutchula kuti Atate wathu ngati timubvomera ndi kumukhulupirira, ndi kutembenuka mtima. M'ndime iyi, taonani anthu amene ali ana a Mulungu.

Yohane 1:12:

Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lake.

3. Kodi anthu onse ndi ana a Mulungu? ____________________

==========================================================

Ngati Mulungu ali Atate wathu, ndiye tidziwa kuti amatikonda ndipo tingathe kulankhula naye za chinthu chilichonse chimenechili mumtima mwathu. Kodi Atate wathu ali kuti? Kodi sali ndi ife nthaŵi zonse? Inde, ali ndi ife. Chikhalirebe pemphero ili likuti, "Atate wathu muli kumwamba." Kodi ndi chifukwa chiyani kukhala choncho? Uku ndiko kutikumbutsa kuti kumwambanso alipo. Ngakhale kuti ndi Atate wathu, Iye ndi Mulungu wamphamvu zonse, Mulungu wa kumwamba ndi wa padziko lapansi. Ichi chitanthauza kuti tizilankhula naye ndi ulemu waukulu.

4. Kodi Mulungu ali kuti? Iye ali ku ____________________

Ndipo alinso pa ________________________________________

==========================================================

Chigawo china cha pemphero chikuti:

<u>Dzina lanu liyeretsedwe.</u>

Kodi tingathe kusonyeza bwanji ulemu wathu kwa Mulungu? Makolo akale anali kupereka madzi kapena mowa kapena nyama. Tingathe kusonyeza ulemu pakumtama chifukwa chaukulu wake, ndi kumuthokoza chifukwa cha madalitso amene Iye amatipatsa.

5. Talembani zinthu zina zimene tingathe kumtama nazo Mulungu.

___________________________________

___________________________________

6. Talembani madalitso amene Iye amatipatsa amene ife tiyenera kumuthokozera.

___________________________________

___________________________________

Tikatha kumuuthokoza ndipo tiyambe kumpempha. Pemphero limene Yesu anaphunzitsa ophunzira ake limati:

<u>Ufumu wanu udze.</u>

<u>Kufuna kwanu kuchitike, monga kumwamba chomwecho pansi pano.</u>

Pano pali chinthu chofunika kwambiri kuchipempha. Tisamangobvutika kwambiri ndi zinthu zathu zokha. Yesu anaphunzitsa ophunzira ake kuti pali china chofunika koposa. Tinaphunzira mmene Iye anakambira izi pa Mateyu 6:33.

7. Kodi chimene chili pa Mateyu 6:33 ndi chiyani chakuti tingakumbukire koposa zinthu zina zonse. Tapezani ndime iyi kuchokera m'Buku Lopatulika ngati simungathe kukumbukira.

___________________________________

==========================================

Tiyenera kupemphera kuti mphamvu ya Mulungu idzalamulire dziko lonse lapansi. Tiyeneranso kupemphera kuti chifuniro chake cha Mulungu chichitike...osati kumwamba kokhako ayi, komanso pansi pano.

8. Kodi Ufumu wa Mulungu tiyenera kuupempherera bwanji?

______________________________________________

************************************************************

MAYANKHO

3. Ayi, sali ana a Mulungu. Ngati munanena kuti inde werenganinso ndime imeneyi. Akuti okhaokha amene anamulandira Yesu, ndiwo ana ake.
1. Muyenera kuyankha funso limeneli.
4. Kumwamba, padziko lapansi.
7. Ufumu wa Mulungu.
5. Izi ndi zinthu monga mphamvu yake yoposa, ndi nzeru zake zakuya, ndipo ali paliponse, ndipo sasintha konse.
2. Tiyenera kuganizira za mawu ndikupemphera ndi mtima wathu wonse.
8. Tiyenera kupemphera kuti chifuniro chake chichitike.
6. Izi ndi zinthu monga chikondi chake, ndi chikhulupiriro chake ndi madalitso a chakudya, nyumba ndi zobvala.

SABATA LA KHUMI: PEMPHERO LA AMBUYE NDI KUBWEREZA
TSIKU LACHIWIRI:

Tikuona zinthu zimene Yesu ananena kwa ophunzira ake za mapemphero.

1. Kodi Yesu anawapatsa chiyani ophunzira ake chowathandiza kudziwa mmene anganenere pamene ali kupemphera?

________________________________________

==========================================================

Werenganinso pemphero lonse.

Mateyu 6:9-13:

Chifukwa chake pempherani inu chomwechi: Atate wathu wa kumwa mba. Dzina lanu liyeretsedwe. Ufumu wanu udze. Kufuna kwanu kuchitidwe, monga kumwamba chomwecho pansi pano. Mutipatse ife lero chakudya chathu cha lero. Ndipo mutikhululukire mangawa athu, monga ifenso takhululukira mangawa athu. Ndipo musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woipayo: Chifukwa wanu uli ufumu, ndi mphamvu, ndi ulemerero wa nthaŵi zonse Amen.

2. Pamene tipemphera, kodi tiyenera kuyamba ndi kupempha kapena kuthokoza?

________________________________________

==========================================================

3. Pamene tipempha, kodi chinthu chofunika kwambiri chimene tiyenera kupempha ndi chiyani?

________________________________________

==========================================================

Koma Mulungu amafunanso kuti ife tizipempha zomwe timafuna.

Mutipatse ife lero chakudya chathu cha lero

Atate wathu amasamalira zofuna zamatupi athu. Iye amatipatsa zinthu zimene ife timazifuna, koma amafuna kuti ife tizipempha. Ndipo Iye amafuna kuti ife tizikumbukira kuti zinthuzo zimachokera kwa Iye.

4. Talembani zinthu zina ziŵiri kupatulapo chakudya zimene tingathe kuzipempherera pa moyo wathu wa tsiku lililonse.

   (1) ______________________________

   (2) ______________________________

==========================================

Mulungu amafunanso kuti tizipempherera zosowa zathu za uzimu.

Ndipo mutikhululukire mangawa athu, monga ifenso tawakhululukira amangawa athu.

Kupempha Mulungu kuti atikhululukire mangawa athu ndicho chigawo chofunika kwambiri pa mapemphero, koma ifenso tizikumbukira zimene ife tiyenera kuchita.

5. Ngati tikufuna kuti Mulungu atikhululukire machimo athu kodi tiyenera kuchita chiyani kwa anthu ena?

   ______________________________

==========================================

Onani kuti pomaliza pa pemphero limene Yesu anaphunzitsa ophunzira ake, palinso mawu otamanda.

Pakuti wanu uli Ufumu, ndi Mphamvu, ndi ulemerero

wa nthaŵi zonse Amen.

Ichi chimatisonyeza kuti pemphero silitanthauza kumangopempha zinthu.

Mulungu sikuti amangofuna kutikhulukukira machimo athu kokha, koma amafunanso kutipatsa chigonjetso cha machimo athu ndi kuti tisaŵapitirizenso.

Ndipo musatitengere ife kokatiyesa, koma mutipulumutse ife kwa woipayo.

Ngati ife titapanga mbali yathu ya mapemphero pa kum'khulupirira Iye ndiye kuti Mulungu adzapanganso mbali yake yotithandiza kugonjetsa mayesero oipa.

1 Akorinto 10:13:
Sichinakugwereni inu chiyeso koma cha umunthu, koma Mulungu ali wokhulupirika, amene sadzalora inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza; koma pamodzi ndi chiyeso adzaikanso populumukira, kuti mudzakhoze kupirirako.

6. Ngati tipemphera kwa Mulungu, kodi Iye adzalora kuti mayeso oipa amene ali opambana mphamvu yathu atigwere ife?

______________________________

==========================================================

Ndipo musatitengere ife kokatiyesa, koma mutipulumutse ife kwa woipayo.

Taphunzira kuti mphamvu ya Satana ndi yolimba ndipo tiyenera kumenyana naye.

7. Kodi tingathe kumenyana naye bwanji Satana?

______________________________

8. Kodi timadziwa bwanji kuti Mulungu adzatithandiza kupambana Satana?

______________________________

==========================================================

Onani kuti pomaliza pa pemphero limene Yesu anaphunzitsa ophunzira ake, palinso mawu otamanda.

> Pakuti wanu uli Ufumu, ndi Mphamvu, ndi ulemerero wa nthaŵi zonse. Amen.

Ichi chimatisonyeza kuti pemphero silitanthauza kumangopempha zinthu.

9. Kodi pemphero ndi chiyani? ______________________

______________________________________________

==========================================================

Mbali yaikulu yakupemphera kwathu izikhala yothokoza ndi kutamanda Mulungu.

10. Pempheroli limanena kuti pali zinthu zitatu zimene zili za Mulungu. Kodi zinthu zimenezi ndi ziti?

    (1) ____________ (2) ____________ (3) ____________

11. Kodi zinthu zimenezi zimakhala zake kwa nthaŵi yotani?

    ______________________________________________

==========================================================

Pali liwu limene timamalizira nalo mapemphero athu nthaŵi zonse. Nthaŵi zonse timanena kuti "Amen." Kodi mumadziŵa zimene liwu limeneli limatanthauza? Mwina mwake mumaganiza kuti ndiyo njira yonenera kuti mapemphero anu atha. Ayi, limatanthauza chinthu china chake. Limatanthauza kuti, "Chilekeni chikhale choncho." Mwa ichi pamene mupemphera ndi pamene munena kuti Amen dziwani kuti pomaliza, muli kunena kuti "Chilekeni chikhale monga mmene ndapemphereramu.

12. Kodi ife tiyenera kupempherera chinthu china chake chimene sitichifuna kuti chichitike?

    ______________

==========================================================

Koma ine ndiganiza kuti nthaŵi zina anthu amapempherera zinthu zimene iwo safuna, chifukwa sapemphera ndi mtima wawo wonse. Pamene tinena kuti, Amen, motsimikiza ndiye kuti tili kupemphera ndi mtima wonse.

13. Kodi liwu lakuti Amen, limatanthauza chiyani?

______________________________________________

**************************************************************

MAYANKHO

9. Kupemphera ndiko kulankhula ndi Mulungu.
7. Pakupemphera.
4. Ichi chingakhale chinthu chilichonse monga ndalama, zobvala, ntchito, kapena mvula.
1. Anawapatsa pemphero.
6. Ayi.
13. Chilekeni chikhale choncho.
8. Iye analonjeza m'Buku Lopatulika kuti adzatero.
10. Ufumu, mphamvu ndi ulemerero.
2. Ndi kuthokoza.
5. Tiyenera kuwakhululukira.
3. Kuti chifuniro chake chichitike.
12. Ayi.
11. Nthaŵi zonse.

SABATA LA KHUMI: PEMPHERO LA AMBUYE NDI KUBWEREZA
TSIKU LACHITATU:

Tsopano ndikufuna kuti ndikupatseni mafunso okuthandizani kukumbukira zonse zimene mwaphunzira m'maphunziro awa. Yankhani mafunsowa monga mmene mukanayankhira pa mayeso. Musayang'anire mayankho mpaka mutatsiriza kuyankha mafunso onse a tsiku limodzi.

Pamene mufuna kuona mayankho, mudzangopeza zizindikiro za masamba amene adzakuuzeni mmene mudzawapezere m'bukumo. Taonani m'buku kuti muone ngati mwakhoza kapena mwalephera. Ngati yankho lanu lili losakhoza, werenganinso tsambalo m'bukumo kuti muone pamene mwachimwira ndi pamene simunamvetsetse bwino. Lembani yankho lanu lokhoza pambali pa yankho lolakwa.

Kubwerezaku kudzatitengera masiku atatu, chifukwa chakuti mukatha mafunso a tsiku limodzi mudzakhala ndi nthaŵi yokonza zimene mwalakwa ndi kuphunzira mayankho abwino.

1. Kodi pemphero ndi chiyani? ______________________

2. Kodi kungopempha zinthu ndi pemphero labwino? ________

3. Pamene tikulankhula ndi munthu wina wake sitingolankhula kokha ayi, komanso tima

   ______________________

4. Talembani zifukwa zitatu zimene ife tiyenera kupempherera.

   (1) ______________________

   (2) ______________________

   (3) ______________________

5. Kodi pemphero limachita chiyani kwa Mulungu? Lembani zinthu ziwiri.

(1) ______________________________

(2) ______________________________

6. Kodi pemphero limatithandiza bwanji? Lembani njira zitatu.

(1) ______________________________

(2) ______________________________

(3) ______________________________

7. Kodi tsiku lililonse Akhristu ambiri amapemphera nthaŵi yanji?

(1) ______________ (2) ______________

(3) ______________ (4) ______________

8. Kodi Mulungu amakhala nafe panthaŵi yanji? ____________

Kodi tingathe kulankhula naye nthaŵi yanji? ____________

9. Kodi kupemphera kwa m'maŵa ndi madzulo, pakudya, ndi banja lonse, ndi pamene mukugwira ntchito, kuli kokwanira?

______________________________

Nanga nthaŵi ina imene mungapemphere ndi iti? ____________

10. Kodi tizipeza malo apatokha kangati tikupemphera ndi Mulungu?

______________________________

11. Kodi malo ena ndi ati amene ife tingathe kupitako ndi kukakhala kwatokha ndi Mulungu?

______________________________

12. Kodi pamene tili ndi mabvuto, kapena chofunika chapadera, kapena cholinga chachikulu, tiyenera kuchita chiyani?

______________________________________________

*****************************************************************

MAYANKHO

| | | |
|---|---|---|
| 11. | Tsamba | 88-90 |
| 8. | Tsamba | 43-46 |
| 5. | Tsamba | 24-26; 34-36 |
| 2. | Tsamba | 7-9 |
| 12. | Tsamba | 52-56 |
| 9. | Tsamba | 43-46 |
| 6. | Tsamba | 27-33 |
| 3. | Tsamba | 83-87 |
| 10. | Tsamba | 48-51 |
| 7. | Tsamba | 38-42 |
| 4. | Tsamba | 20-37 |
| 1. | Tsamba | 5:19 |

SABATA LA KHUMI: PEMPHERO LA AMBUYE NDI KUBWEREZA
TSIKU LACHINAYI:

1. Kodi tiyenera kumayamba bwanji mapemphero athu?

________________________________________

2. Kupatulako kulankhula, kodi tiyenera kuchita chiyani tikamapemphera?

________________________________________

3. Kodi tizipempherera ayani? Lembani maina a anthu asanu.

__________ __________ __________

__________ __________ __________

__________ __________ __________

4. Nanga ife tizipempherera chiyani mwa ife tokha? Lembani zinthu zinayi.

__________ __________

__________ __________

5. Kodi zinthu zofunika kwambiri pakati pa zinthu izi ndi ziti?

________________________________________

________________________________________

6. Kodi tingadziŵe bwanji anthu oyenera kuŵapempherera m'mudzi mwathu?

________________________________________

________________________________________

7. Kodi nchifukwa chiyani tiyenera kupempherera atsogoleri athu?

______________________________

______________________________

8. Kodi timadziŵa bwanji kuti tizipempherera Akhristu ena?

______________________________

______________________________

9. Kodi tingathe kugwiritsa ntchito chiyani pomenyana ndi Satana?

______________________________

10. Kodi tikamamenyana ndi Satana, ndi chinthu chachikulu chiti chimene ife tiyenera kupempha?

______________________________

______________________________

11. Kodi tizipemphera bwanji? Lembani njira zinayi.

(1) ______________________________

(2) ______________________________

(3) ______________________________

(4) ______________________________

12. Kodi kugwada ndiyo njira yokhayo yopempherera?

______________________________

13. Kodi kubwereza-bwereza mawu kumathandiza kuti Mulungu atimvere?

______________________________

14. Kodi njira yabwino ndi iti yakuti inu mupeze chinthu choyenera kuchipempherera?

_______________

15. Lembani nthaŵi imene mapemphero ataliatali ali ofunika, ndi nthaŵi imene sali ofunika.

_______________

_______________

16. Kodi ndi chifukwa chiyani tiyenera kupemphera m'dzina la Yesu? Perekani zifukwa ziwiri.

(1) _______________

(2) _______________

17. Kodi chimalepheretsa mapemphero athu kuyankhidwa ndi chiyani? Lembani zifukwa zisanu.

(1) _______________

(2) _______________

(3) _______________

(4) _______________

(5) _______________

18. Kodi tiyenera kuchita chiyani pa nthaŵi ya kupemphera ngati titapeza tchimo m'mitima mwathu?

_______________

19. Kodi Mulungu amatipatsa yankho la mtundu wanji ngati tipempha zinthu modzikonda tokha?

_______________

_______________

20. Kodi ndi chifukwa chiyani mayankho a mapemphero athu nthaŵi zina amachedwa kubwera? Perekani zifukwa

(1) ______________________________

(2) ______________________________

*************************************************************

MAYANKHO

| | | |
|---|---|---|
| 1. | Tsamba | 56 - 59 |
| 2. | Tsamba | 10 |
| 3. | Tsamba | 64 - 66 |
| 4. | Tsamba | 60 - 62 |
| 5. | Tsamha | 60 - 62 |
| 6. | Tsamba | 66 |
| 7. | Tsamba | 66 |
| 8. | Tsamba | 69 |
| 9. | Tsamba | 74 - 76 |
| 10. | Tsamba | 74 - 76 |
| 11. | Tsamba | 79 - 84 |
| 12. | Tsamba | 90 |
| 13. | Tsamba | 90 |
| 14. | Tsamba | 83 |
| 15. | Tsamba | 91 - 153 - 155 |
| 16. | Tsamba | 98 |
| 17. | Tsamba | 101 - 124 |
| 18. | Tsamba | 101 - 105 |
| 19. | Tsamba | 110 - 113 |
| 20. | Tsamba | 123 - 124 |

SABATA LA KHUMI: PEMPHERO LA AMBUYE NDI KUBWEREZA
TSIKU LACHISANU:

1. Kodi ndi mayankho angati amene tingapeze amapemphero athu popanda chikhulupiriro?

_______________

2. Kodi tingawerenge chiyani m'Buku Lopatulika kuti chikhulupiriro chathu chikhale cha mphamvu? Lembani zinthu ziwiri.

(1) _______________

(2) _______________

3. Lembani Mateyu 7:7. _______________

_______________

_______________

_______________

4. Ngati tisanthula mitima yathu ndipo Mulungu akatisonyeza kuti ili yoyera, kodi chimachitika ndi chiyani ku chikhulupiriro chathu?

_______________

5. Kodi tingapemphe ndani kuti chikhulupiriro chathu chikhale cha mphamvu?

_______________

6. Yesu anati chikhulupiriro chathu chingathe kukhala ngati

_______________

7. Ngati chikhulupiriro chathu chili chochepa, kodi tichiyembekeze kuti chikule tisanayambe kupempha zinthu?

_______________

8. Kodi ndi chifukwa chiyani kuli kwabwino kupempherera pamodzi m'magulu?

9. Lembani Mateyu 18:19-20:

10. Kodi mpingo uyenera kupemphera bwanji pamene pali mabvuto kapena zosoweka zazikulu?

11. Kodi ana amaphunzira bwanji kupemphera?

12. Kodi kupemphera pamodzi kumathandiza bwanji pa banja?

13. Kupatulako kupemphera pamodzi ndi mpingo kapena banja lanu, kodi gulu lina limene mungathe kupemphera nalo ndilo liti?

14. Kodi Yesu anaŵapatsa chiyani ophunzira ake chowathandiza kupemphera? ______________________________

______________________________

15. Mpemphero limeneli, kodi Yesu anawauza dzina lanji kuti azigwiritsa ntchito potchula Mulungu?

______________________________

16. Asanayambe kupempha zinthu, kodi Yesu anawauza kuti azinena chiyani? ______________________________

______________________________

17. Kodi tiyenera kumpempha Mulungu zosowa zathu za tsiku ndi tsiku monga chakudya, ndi zobvala? ______________

18. Ngati wina atichimwira, kodi tiyenera kuchita chiyani kuti Mulungu amve mapemphero athu?

______________________________

19. Kodi Mulungu adzalekerera kuti mayesero amphamvu koposa ife atigwere? ______________

20. Kodi tiyenera kupemphera kuti chichitike ndi chiyani pa dziko lapansi? ______________________________

21. Kodi ndani ali ndi ufumu, mphamvu ndi ulemerero?

______________________________

22. Kodi liwu lakuti "Amen" limatanthauza chiyani? ________

*******************************************************************

MAYANKHO

1. Tsamba 125 - 129
2. Tsamba 125 - 133
3. Pezani ndime imeneyi m'Buku Lopatulika ndipo muone ngati mwalemba bwino.
4. Tsamba 134 - 136
5. Tsamba 137 - 139
6. Tsamba 141
7. Tsamba 138 - 139
8. Tsamba 146
9. Pezani ndime imeneyi m'Buku Lopatulika ndipo muone ngati mwalemba bwino.
10. Tsamba 149 - 152
11. Tsamba 158 - 160
12. Tsamba 160 - 162
13. Tsamba 163 - 167
14. Tsamba 180 - 182
15. Tsamba 180 - 182
16. Tsamba 182 - 183
17. Tsamba 184 - 186
18. Tsamba 184 - 186
19. Tsamba 184 - 186
20. Tsamba 182 - 183
21. Tsamba 182 - 188
22. Tsamba 186 - 188

M'NDANDANDA WA MABUKU AMBIRI OCHOKERA KU EVANGEL

Evangel Publishing House amagwirizana ndi AEAM Theological Commission kudinda mabuku opitirira pa chiwerengero cha makumi aŵiri (20) kuti agwiritsidwe ntchito kwa magulu a ophunzira za Mawu a Mulungu m'madera osiyanasiyana. Ena mwa iwo atha kale kulembedwa pakali pano. Ambiri mwa iwo atsala pang'ono kutha. Zili kuyembekezeka kuti mabuku okwanira makumi aŵiri (20) adzadindidwa pakutha kwa chaka cha 1974.

Evangel Publishing House adzakhala okondwa kwambiri pokuikani inu mu m'ndandanda wawo wotumiza mabuku kuti adzakudziwitseni za mabukuwa akadzatha kulembedwa. Tilembereni ife kalata pa kutipatsa maina aku malo ophunzirirapo Buku Lopatulika, sukulu yapamwamba, mpingo kapena nyumba yogulitsilamo mabuku.

MABUKU WOLEMBEDWA PA MWEZI WA MARCH 1973
Kulankhula ndi Mulungu
Kubweretsa Anthu kwa Yesu

BUKU LOLEMBEDWA PA MWEZI WA JUNE 1973
Kufufuza za m'Chipangano Chatsopano, Gawo Loyamba

MABUKU OLEMBEDWA KUMAMALIZIRO KWA CHAKA CHA 1973
M'busa ndi Ntchito Yake
Kakulidwe ka Mpingo
Kachitidwe ka Chikhristu

MABUKU OLEMBEDWA M'CHAKA CHA 1974
Kufufuza za m'Chipangano Chatsopano, Gawo Lachiŵiri
Kufufuza za m'Chipangano Chatsopano, Gawo Lachitatu
Kufufuza za m'Chipangano Chakale, Gawo Loyamba
Kufufuza za M'Chipangano Chakale, Gawo Lachiŵiri
Kufufuza za m'Chipangano Chakale, Gawo Lachitatu
Makalata kwa Onse
Akorinto Woyamba
Maphunziro a Ulaliki
Nthaŵi ndi Maiko a Buku Lopatulika
Agalatiya
Maphunziro a pa Sabata (Sundy School)
Yesaya
Karko
Yohane

KULANKHULA NDI MULUNGU

Ili ndi buku loyamba kulembedwa mu Afrika muno. Bukuli linalembedwa pofuna kuthandiza mipingo ya mu Afrika. Komanso linalembedwa m'njira yoti likhoza kugwiritsidwa ntchito pa nthaŵi ya maphunziro a Buku Lopatulika (Bible Study) ndi pa zokambirana za sabata ndi sabata. Njira yomwe bukuli linalembedwera imatchedwa malangizo okonzedweratu (Programmed Instructions). Njira yophunzitsira kupyolera m'zokambirana za sabata ndi sabata imatchedwa Maphunziro a Mawu a Mulungu Otumizidwa kwa Ophunzira (Theological Training by Extension.

KULANKHULA NDI MULUNGU ndi buku loyamba m'ndandanda wa mabuku opyolera makumi aŵiri amene akukonzedwa ndi Bungwe la Evangelicals of Afrika and Madagascar (AEAM) lomwe poyamba linkatchedwa kuti Theological Commission (AEBICAM).

Ntchito ya mndandanda wa mabuku ameneŵa, ndi kuphunzitsa atsogoleri a mipingo. Mabukuŵa akhoza kugwiritsidwa ntchito ku sukulu za Buku Lopatulika ngakhale malo ena a T.E.E. Mipingo yambiri imaitanitsa aphunzitsi amene ali oyenera kuphunzitsa maphunziroŵa. Aphunzitsiwa amapita ku mpingoyi kamodzi pa sabata. Mayeso amachitika pakutha pa sabata iliyonse.

Anthu omwe akufunitsitsa kudziŵa zambiri za choonadi cha Mulungu akhoza kuphunzira bukuli kunyumba kapena kupanga gulu pakumakumana kamodzi ndi kukambirana sabata iliyonse. Olemba bukuli ali okonzeka kuthandiza anthu amene akufuna kuyambitsa magulu otere.

Njira ya malangizo amene alembedwa m'mabukuŵa ndi maganizo a Maphunziro a Mawu a Mulungu Otumizidwa kwa Ophunzira a theological training by extension ndipo ayesedwa m'maiko ambiri mu Afrika. Maphunzirowa atayesedwa anaoneka kuti ndi njira yabwino kwambiri yophunzitsira atsogoleri m'mipingo.

Buku ili la KULANKHULA NDI MULUNGU ndi lobwerezedwanso. Kusinthika kunachitika m'buku lonse pofuna kuti uthenga umveke bwino ndiponso kuti malangizo okonzedweratu agwiritsidwe ntchito bwino.